## NYONGOLOTSI ZA M'MIZU YA TOMATO (MANDOLO)

**ROOT-KNOT NEMATODE OF TOMATO**



Mizu ya tomato kutupa chifukwa cha nyongolosi[a], ndikupagisa kuti masamba a tomato aume[b] © *CABI/Plantwise*

Nyongolotsi za m'mizu ya tomato ndi mtundu wa Nyongolotsi zing'onozing'ono zomwe zimakhala mu nthaka. Nyongolotsizi zimalowa m'mizu ya tomato kumamwa michere yomwe mizuyi imatenga mu nthaka. Izi zimapangitsa kuti tinjira todutsamo michere titsekeke.

Tomato ogwidwa ndi nyongolotsizi amakhala pachiopsezo chogwidwa ndi tizilombo komanso matenda ena. Izi zimachepetsa zokolola.

Nyongolotsizi zimagwiranso mbewu zina monga nyemba, mabilinganya ndi mbatata ya kachewere/mbatatesi.

### MOYO NDI KAKULIDWE KA NYONGOLOTSI ZA M'TOMATO


Nyongolotsi yaikazi ingathe kuikira mazira okwana 600. Mazira angathe kukhala mu nthaka kwa zaka zoposera 5.

Mazira akaswa, tinyongolotsi timayenda ndi chinyezi m'nthaka ndikulowa m'mizu ya tomato. Mkati mwa mizuyi tinyongolotsi timakatseka tinjira tobweretsa michere kuchoka ku mizu kufika ku thunthu titakula.


Pakatha masiku angapo (7-12) tinyongolotsi timayamba kuikira mazira. Nyongolotsi zimakhala moyo kwa masiku pafupifupi 25.

## ZIZINDIKIRO ZAKE

Mbewu imafota ndikuchita chikasu komanso imapinimbira. Mtengo wa tomato ukazulidwa, mizu yake imakhala ndi totupa tofanana ndi mandolo/thuku/maphulubudu.




*Masamba ofota komanso ochita chikasu chifukwa cha nyongolotsiza m'mizu ya tomato © DARS*




*Mizu yotupa yogwidwa ndi nyongolotsi © CABI/Plantwise*

**NJIRA ZOCHEPETSERA NYONGOLOTSI M'TOMATO**

Pofuna kuchepetsa vuto la nyongolotsi ku tomato tsatirani izi:

- Yenderani munda wa tomato pafupipafupi
- Bzalani mbewu zopilira ku nyongolotsi
- Wotchani nthaka yomwe igwiritsidwe ntchito ngati nazale
- Bzalani mbewu mwakasinthasintha
- Wokerani mbewu za thanzi
- Palirani ndi kuchotsa mbewu zomera zokha
- Pewani kugwiritsa ntchito madzi ochokera malo omwe kuli vuto la nyongolotsizi
- Zulani ndi kuotcha mbewu zogwidwa ndi nyongolotsi
- Gwiritsani ntchito manyowa
- Gaulani mukangomaliza kukolola kuti mizu iwume
- Poperani mankhwala ovomerezeka anyongolotsi za m'dothi (Nematicides). Samalani pogwiritsa ntchito mankwala chifukwa angathe kuononga moyo.

**DZIWANI IZI**; Kuchepetsa chiwelengero cha tinyongolotsi ndikotheka ngati mutagwilitsa ntchito njira zosiyanasiyana zotetezera tizirombo nthawi imodzi (IPM).

Mukafuna kudziwa zambiri, funsani alangizi azamalimidwe a m'dera lanu

**Malawi**
**Created/Edited on October 9, 2025**

©MINISTRY OF AGRICULTURE, MADIPHS PROJECT,
CC BY-NC-SA 4.0 LICENCE